

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

KUTUMIZA ANTHU OYENERERA

Mzaka za pafupifupi 759 BC, Yesaya anamva liwu kuchokera kwa Ambuye ndipo anamufunsa kut: "Ndidzatumiza yani, ndipo ndani adzatimukira ife?" (Yesaya 6:8). Kodi ndi ndani amene adzatenge Mau a Mulungu ndi kukawagawira kwa anthu amene akuwasowa kwambiri? Ndani kodi amene avomere kuperekwa nthawi yake ndi luso lake, ndi kusiya zonse za mdziko kuti adzipereke yekha ku utimiki ndi ntchito ya Mulungu? Ndani angalolere kuti asatchukenso kapena asadziwikenso ndipo akhale m'moyo wa totomoyo ndi cholinga chakuti akalankhule mosanyengerera uthenga wochokera Kumwamba? Ndani nanga kodi amene akulolera kuti akanidwe ndi kunyozedwa kapenango kusekedwa chifukwa cha Uthenga Wabwino? Ndani nanga amene agwiritsitse choonadi chodabwitsa cha chiyero ndi chiyembekezo? Yesaya anamva kuyitana kwa Mzimu ndipo anayankha kuti: "Ndine pano; munditumize ine" (Yesaya 6:8).

"Zotuta zichulukadi koma antchito ali owerengeka" (Mateyu 9:37). Mulungu akufuna anthu oyenerezeka ndi okhulupirika kuti adzipereka okha ngati nsembe zamoyo pa guwa, kudzipereka moyo wawo pa kufalitsa uthenga wa

muyaya ndi wa chipulumutso ku dziko lino limene likutayika. Mulungu ali ndi mayitanidwe komanso malo apaderadera kwa aliyense mu thupi la Khristu. Ngakhale kuti atumiki, aphunzitsi ndi alaliki a uthenga wabwino akufunikira kwambiri,



komabe Mulungu amafuna kuti atumiki akhale woyenerezeka ku uzimu.

Mulungu akufuna antchito amene akhale zitsanzo za tanthauzo la mmene munthu angakhalire m'moyo wachiyero ndi wodzipatula mu dziko lino loyipali. "Wam'munda wogwiritsitsa ntchitoyo ayenera akhale woyamba kulandira zipatsozo (2 Timoteo 2:6). Pofuna kuti ayigwire bwino ntchito ya Mulungu, nkofunikira kuti mtumikiyo akhale ali ndi umboni wakuti anapulumukadi. Kuchokera pa maziko amenewa, iye

akhoza kulankhula molimba mtima ndi motsimikizika. Asanatuluke kukagwira ntchito ya Mulungu, nkofunikira kuti munthu adzadzidwe ndi mphamvu za Mzimu Woyer (Machitidwe 1:8). Mzimu ndiye amene amatitsogolera pamene tikugwira ntchito imene Mulungu anatitayanirayo. Mzimuyo amapereka chitonthozo, cholinga, ulamuliro wakumwamba ndiponso kudzodza.

Munthu wa Mulungu woonadi adzatumikira modzichepetsa, ndi malingaliro ofuna utumiki, osati chifukwa chofuna chuma, ulemu kapena mphamvu (1 Petro 5:2-3). Iye ayenera kukhala chitsanzo cha kwa gulu la nhosa la Mulungu (1 Timoteo 4:12) ndipo ayenera kukwanirtsa m'ndandanda wochokera mu baibulo wa zowayeneresa anthu kuti akhale oyang'anira kapena akuluampingo monga alembra pa 1 Timoteo 3:1-7 ndi pa Tito 1:7-9. Iye akuyenera kukhala wopanda chilema, wakhalidwe labwino, wa mbiri yabwino, wachiyero, wolongosoka, wodziletsa, wofatsa, wolimbikira, wodzisunga, wokhulupirika, wosakonda ndeu ndi wokonda kuchereza alendo. Ngati ali pabanja, akuyenera kukhala mwamuna

(Yapitirira pa tsamba 2)

ZIMENE BAIBULO

Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyerā

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyoero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritsō

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyoero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhaliidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba !)

wa mkazi mmodzi basi ndipo nyumba yake ikhale yolemekezeka. Sakuyenera kukhala wokonda ndeu (2 Timoteo 2:24), kapena watsankho pochita zinthu (1 Timoteo 5:21), kapenango wokonda kuledzera.

Si kofunikira kokha, komatu moyenera ndithu, kuti mtumiki wa Mulungu akhale ndi mphatso yodziwa kuphunzitsa bwino (2 Timoteo 2:24) ndipo adziwe kusanthula bwino chiphunzitso komanso mau a moyo (2 Akorinto 3:5-6). Kumakhala kovuta kuti anthu amvetsere kwa woyimba amene satha kuyimba, kwa mphunzitsi amene satha kuphunzitsa komanso kwa mlaliki amene satha kualikira. Anthu atumikire molingana ndi mphatso imene Mulungu anawapatsa ndipo asamalitse kuti asatulukemo mmenemo.

“Koma tsopano, Mulungu anaika ziwalo zonzezo m’thupi, monga anafuna” (1 Akorinto 12:18). Atumiki enieni amayitanidwa ndi Mulungu, osati mwa kufuna kwa munthu, kapena kuhumba kwawo. Iwo amayenerezedwa ndi Mzimu. Osati chifukwa cha maphunziro awo.

Liwu la Ambuye likuyitanabe, Mzimu wa Mulungu akufunafunabe wina wake avomere mayitanidwe akumwamba akuti apite ku dziko lonse lapansi ndi kualalikira Uthenga wabwino kwa cholengedwa chilichonse (Marko 16:15). Palibenso mayitanidwe ena aakulu kuposa awa, palibenso china chabwino chimene tingatsatire, koposa kuvomera ku kuyitana kwa Mulungu ndi kugwira ntchito yotumikira miyoyo m’munda mwake.

—mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikidwa m’dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwahazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudazazidwa ndi Mzimu Woyerā kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamu; komanso tikhale ndi chiyoero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & René Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu illiyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m’maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zafulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

Mau a Mkonzi



Ndipo iwo adzaitana bwanji pa lye amene sanamkhulupirira? Ndipo adzakhulupirira bwanji lye amene sanamva za lye? Ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? Ndipo adzalalikira bwanji, ngati satumidwa? Monganso kwalembewa, Okometsetsa ndithu ali mapazi a iwo akulalikira Uthenga Wabwino wa zinthu zabwino. —Aroma 10:14-15

Ndiyamika Mulungu chifukwa cha atumiki amene akulolera kuyika moyo wawo pachiswe chifukwa cha uthenga wabwino. Iwo analandira masomphenya kuchokera kumwamba ndipo anagwira ntchito yolalikira za chiyembekezo ndi maweruzo a Mau a Mulungu mokhulupirika. Uthenga wabwino umasinta miyoyo ndipo mkaati mwa mdima wa zochitika a m'dziko lathuli, nkofunikabe kuti tilalikirebe choonadi. Dziko lachipembedzoli ladzadza ndi aneneri ndi atumiki onyenga amene amalalikira uthenga wakuti mukapulumuka zikuyenderani ndipo salalikira uthenga weniweni wa kulapa ndi wa chiyero. Choonadi chonse chimene chili chosadetsedwa chikadali ndi mphamvu yomasula anthu kuchokera ku uchimo kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu.

Ulendo uno mtolo umene Ambuye wandisenzetsa uli pa mutu wa utumiki. Nkofunikira kwambiri kuti antchito oyenerezeka avomere kuyitana kwa Mulungu ndi ntchito yavo mu utumiki. Moyo wa chiphamaso wachuluka kwambiri pakati pa opembedza ndipo chifukwa cha chimenechi chikhristu chanyozedwa kwambiri. Tiyenera tikumbukire za zowayenereza atumiki zimene baibulo limanena ndipo ngati mpingo tizigwitsitse. Tisalolere kuti mbiri chabe, abwenzi, kapena zochitika ku banja kwathu zitipangitse kuti tisulutse muyeso umenewu wochokera mu Baibulo. M'masiku ano, ndi koyenera ndithu kuti atumiki amene ali ndi udindo wotsogolera akhale m'moyo wodzichepetsa ndi wodalira pa Ambuye. Mu mpingo wa Church of God, aliyense ndi wofanana ndi mnzake ndipo palibe wofunikira kwambiri chifukwa cha ichi nkofunikira kuti pamene pali ntchito iliyonse, atumiki asadziona ngati ali pamwamba pa ena onse kapena udindo wao sukuwalola kugwira ntchitoyo.

Atumiki amadutsa mu nyengo zosautsa, komabe palibe chintha china chokoma kuposa kutumikira pansi pa kudzodza kwa Mzimu Woyeria. Ambuye watidalira kuti tikafalitse uthenga uwu wabwino ndipo tifunikira kuti tikalimbikitsidwenso kuti tikweze mau athu ngati lipenga ndi kupereka uthenga wa choonadi mosanyengerera. Nthawi zambiri anthu amene akulalikidwa uthenga amakhala okonzeka kunoza ndi kumuchita chipongwe mlaliki kuposa kuvomereza poyeria kuti sakufuna kulandira uthenga wa choonadi. Atumiki akuyenera kukhala ndi kulimba mtima kochokera kwa Mzimu Woyeria ndipo apitirire kulalikira choonadi. Uthenga wonyengerera ukhoza kubweretsa moyo wonyengerera ndipo uthenga wongofuna kusangalatsa anthu umapangitsa kuti anthu angosangalala basi. Nkofunika ndithu kuti utumiki usatekeseka kupta kumanja kapena kumanzere.

Takambanso pang'ono za kupatulidwa mu m'kalata ino. Kupatulidwa ndi chipunzitso chochokera m'Baibulo ndipo nkofunikira kuti atumiki ndi oyera mtima onse amvetsetse phindu lake. Pamene ena amachoka pa chipunzitsochi chifukwa chakuti chikhoza kuwonetsa kuti pali nyengo zovuta, tiyenera kukhala wokhulupirika komanso tisalole kuti chipunzitsochi ndi machitidwe ake zitayike chifukwa cha mantha. Ndi mdalitso waukulu pamene tizindikira ndi kupatula atumiki amene ali wokhazikika mu chipunzitso ndi mu mzymu.

Michael W. Smith

July 2016

Zambiri Zili pa
INTANETI

*Mukafuna kutipeza
pa intaneti, mulembe
www.thegospeltruth.org
kuti mudzilandira
makalata athu kapenango
kuti muone makalata
akale.*



MUYESO WA BAIBULO OWAYENEREZA ATUMIKI

Machitidwe 1:8 **Odzazidwa ndi Mzimu Woyeria** (Luka 24:49).

2 Timoteo 2:24 **Wokhoza kuphunzitsa**
(1 Timoteo 3:2).

2 Akorinto 3:5-6 **Wokwanira**
(Tito 1:9).

2 Timoteo 2:6 **Woyamba kalandira nawo zipatsozo**

I Petro 5:2-3 **Wa maganizo abwino.**

Wachitsanzo kwa gulu la nkhosa
(1 Timoteo 4:12).

Machitidwe 20:19 **Wodzichepetsa**

1 Timoteo 3:1-7 & Tito 1:7-9
Wopanda chirema, wa makhalidwe abwino, mwamuna wa mkazi mmodzi, woyang'anira bwino nyumba yake, wokonda kuchereza alendo, wosaledzera naye vinyo, asakhale wophunzira kumene, wofatsa, wosakonda ndeu, wakuti ena amchitira umboni wabwino, osati waliuma, wosapsa mtima msanga, wokonda zokoma, wolungama, opanda chiwawa, woyeria mtima, wodziletsa, wokhulupirika.

KUSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: UTUMIKI

Kuwerenga Mau a Mulungu: Ndipo lye anapatsa ena akhale *atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima kuntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu. – Aefeso 4:11-12

Kunena mwachidule: Atumiki, amayitanidwa ndi Mulungu, ndipo ayenera kukhala oyenerezeka, okwanira komanso achitsanzo kwa okhulupirira. Iwo akuyenera kulalikira mokhulupirika ndi kuchenjeza anthu mu choonadi ndi m'chikondi pansi pa kudzodza kwa Mzimu Woyeria.

I. Kutumidwa ku Utumikiwo

- A. Mateyu 28:19-20 Pitani ndipo mukaphunzitse.
- B. Marko 16:15-16 Mukalalikire Uthenga wabwino ku dziko lonse lapansi.

II. Cholinga cha Utumiki

- A. 2 Akorinto 5:20 Akazembe a Khristu.
- B. 1 Akorinto 4:1 Adindo onyamula zinsinsi za Mulungu.
- C. Afilipi 1:7 Kuteteza Uthenga wabwino.

III. Udindo wa pa Utumiki (Chipangano Chakale)

- A. Yesaya 58:1 Fuulani kwambiri, musasiye.
- B. Yesaya 62:6-7 Alonda okhala pa malinga.
- C. Yeremiya 23:1-5 Abusa a nkhosa okhulupirika.
- D. Ezekiele 3:17-21 Ovomerezeka kuti akachenjeze.

IV. Ntchito yolalikira Mau

- A. Aefeso 3:8-9 Lalikilani zinsinsi za ulemelero wa Khristu.
- B. Machitidwe 5:19-20 Lankhulani mau onse a moyo uno.
- C. Machitidwe 20:26-31 Lengezani za nzeru zonse za Mulungu; Yang'anirani ndipo dyetsani mpingo, khalani tcheru, chenjezani.
- D. Tito 2:15 Limbikitsani ndipo dzudzulani ndi ulamuliro wonse.

V. Kalalikidwe kwake

- A. 2 Akorinto 4:5 Lalikirani Yesu, osati za ifeyo.
- B. 1 Akorinto 2:1-5 Osati ndi mau oshashalika a nzeru za anthu, koma ndi mphamvu.
- C. 1 Petro 4:11 Lankhulani molingana ndi mau a Mulungu ku ulemerero wake.
- D. Aefeso 4:15 Lankhulani choonadi mwa chikondi.
- E. Machitidwe 20:20, 27 Musasiye mau ena aliwонse.
- F. 1 Atesalonika 2:4-5 Musakhale okondweretsa anthu. (Agalatiya 1:10-11).
- G. Mateyu 10:28 Lalikirani mosaopa anthu.
- H. 2 Akorinto 3:12 Gwiritsani mau omveka bwino lomwe.

VI. Ntchito Zina za Utumiki

- A. 1 Atesalonika 5:14 Chenjezani, limbikitsani, thandizani, khalani odekha.
- B. 2 Timoteo 2:15 Phunzirani, lingalirani ndipo konzekerani (1 Timoteo 4:14-16).
- C. Mateyu 10:7-8 Perekani kwalulere.

Mau Omaliza

Lalikira mau; chita nao pa nthawi yake, popanda nthawi yake; tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi chiphunzitso...Koma iwe, khala maso m'zonse, imva zowawa, chita ntchito ya mlaliki wa Uthenga Wabwino, kwaniritsa utumiki wako.

2 Timoteo 4:2-5

UTUMIKI

Kuyitanidwa ndi Mulungu


Mzimu wa Mulungu ndiye amene amayitana ndi kuyenereza atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi. Utumikiyo umaperekedwa “kuti akonzere oyera mtima kuntchito ya utumiki ...kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikirito cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu” (Aefeso 4:12-13). Yesu anatuma ophunzira ake, ndipo lero amachitanso momwemo, kuti apite ku dziko lonse lapansi ndi kukalalikira uthenga wabwino (Marko 16:15-16). Umenewu ndi utumuki wofunikia kwambiri polalikira Mau a Mulungu, popeza timatalikira kwa miyoyo ya anthu amene mizimu yawo idzakhala ya muyaya. “Mauwa ali okhulupirika, ngati munthu akhumba udindo wa woyang'anira[mbusa/mkuluwampingo], aifuna ntchito yabwino” (1 Timoteo 3:1). Imeneyi si ntchito imene tingayitengere mwachibwana kapena moseweretsa ayi, koma ndi utumiki umene zotsatira zake ndi mayitanidwe a Mulungu komanso kudzodza kwa Mzimu Woyerwa m'moyo wa munthu.

Antchito oyenerezeka

Atumiki akuyitanidwa kuti akhale akazembe a Khristu ndipo iwo amuyimirire iye mu gawo lililonse la moyo. Nkopunkira kwa utumikiyo kuti “muyende koyenera maitanidwe amene munaitanidwa nao” (Aefeso 4:1). Iwo ayenera kubweretsa ulemerero kudzina la Khristu kudzera mu m'moyo wao, machitidwe awo, mavalidwe awo ndi kakkhalidwe kawo. Atumiki amene sali oyenerezeda malingana ndi Malemba sakuyenera kugwira ntchito ya utumiki mpakana nthawi iyo imene ayesedwa okwanira pa muyeso wa mu Baibulo komanso kuti anayitanidwa ndi Ambuye. Atumiki amawadalira kuti akhale “adindo a zinsinsi za Mulungu” (1 Akorinto 4:1) ndipo kuti akhale oteteza chikhulupiriro.

Ntchito ya Mulungu pa dziko lonse yakhala ikubwerera m'mbuayo chifukwa cha utumiki onyenga ndi anthu osavomerezeka amene amanyamula Mau a Mulungu. Chipembedzo changokhala ngati bizinesi kwa utumiki ambiri. Atumiki enieni amatumikira anthu. Ntchito ya Mulungu pa dziko lonse yabwerera m'mbuayo chifukwa cha utumiki onyenga ndi

iwo osayenerezeka amene agwira ntchito yolalikira Mau a Mulungu. Chipembedzo changokhala ngati bizinesi kwa atumiki ambiri. Atumiki enieni a Mulungu amatumikira anthu, osati kugwira ntchito kuti adzilemeretse koma kuti alimbikitse miyoyo ya anthu. “Wetani gulu la Mulungu lili mwa inu, ndi kuliyan'ania, osati mokakamiza, koma mwafulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwachangu; osati monga ochita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo” (1 Petro 5:2-3). “Munalandira kwaulere, patsani kwaulere” (Mateyu 10:8).



Alonda okhala pa malinga

Chipangano Chakale chimaperekira langizo lomveka bwino komanso loyenerera kwa iwo amene akutumikira. “Ndaika alonda pa malinga ako, Yerusalem; iwo sadzakhala chete usana pena usiku; inu akukumbutsa Yehova musakhale chete” (Yesaya 62:6). “Fuula zolimba, usalekerere, kweza mau ako ngati lipenga, ndi kuwafotokozena anthu anga cholakwa chao, ndi banja la Yakobo machimo ao.” (Yesaya 58:1). Mulungu wayika atumiki kuti akhale ngati alonda pa malinga kuti potero alalikire uthenga wabwino wamuyaya umene uli ngati mchere wokometsa moyo ku moyo ndi wowawitsa imfa ku imfa. Ngati mtumiki awona mdaniyo akugwira ntchito pakati pa anthu ndipo ngati sayimba lipenga ndi kuchenjeza, anthu amene adzatiyikewo

adzawerengeredwa pa mutu pake (Ezekiele 3:17-21). Koma ngati mtumiki alengeza uthenga wochokera kwa Mulungu komabe anthu ndi kutayika, iye sadzayimbidwa mlandu chifukwa cha tchimo ndi kusamvera kwavo. Ndi chinthu choopsa kwambiri kuti munthu adzitchule kuti ndiye mtumiki wa Ambuye, popeza anthu amayembekezer zambiri kuchokera kwa iye.

Udindo wolalikira Mau

Atumiki akuyitanidwa kuti alalikire za chuma chosalondoleka cha Khristu (Aefeso 3:8) ndi kunena “kwa anthu onse mau a Moyo umene” (Machitidwe 5:20). Chimakhala chimwemwe ndi mwayi kulalikira uthenga wa chiyembekezo ndi chipulumutso kudzera mwa Yesu Khristu. Atumiki ayenera kukhala ngati Paulo amene ananena kuti “Pakuti sindinakubisirani pakukulalikirani uphungu

(Yapitirira pa tsamba 6)

wonse wa Mulungu" (Machitidwe 20:27). Kulalikira choonadi kudzapangitsa kuti ena atsutsane nanu, amkati ndi akunja omwe, koma atumiki akuchenjezedwa kuti akhale okhulupirika ndipo "Izi lankhula, ndipo uchenjeze, nudzudzule ndi ulamuliro wonse" (Tito 2:15). Atumiki asalalikire kuti akondweretse anthu koma kuti akondweretse Mulungu (1 Atesalonika 2:4-5). Mauthenga asalalikidwe poopa munthu (Mateyu 10:28) kapena za masautso amene angabwere kutsogoloko.

Dyetsani gulu la nkhosa


Mulungu anawayika atumiki kuti akhale oyang'anira auzimu ndipo iwo ayenera kuukwanirtsa udindowo osati ngati olamulira koma monga otumikira kapena abusa. Lwo akuwuzidwa "kuti muwete Mpingo wa Mulungu" (Machitidwe 20:28) powupatsa chakudya choyenera ndi chokwanira bwino. Atumiki ayenera kulalikira Uthenga Wabwino ndi kulankhula zochokera kwa Mulungu ku ulemerero wake (1 Petro 4:11). Atumiki ayenera kusamalitsa kuti asalalikire za m'maganizo mwao, kapena miyambo chabe komanso kuchokera ku mbiri, komatu alalikire kuchokera ku maziko a Mau a Mulungu oyera ndi osasinthika.

Atumiki ambiri amafuna kudzitchukitsa iwo eni ndi kufuna kukopa anthu kwa iwo pongowasangaltsa, pogwiritsa ntchito moyo wachikoka ndi nzeru zaku sukulu. Mtumiki weniweni wa Khristu amazindikira kuti "kukwanira kwathu kuchokera kwa Mulungu; amenenso anatikwanirtsa ife tikhale atumiki a pangano latsopano;"

(2 Akorinto 3:5-6). "Pakuti tilalikira si za ife tokha, koma Yesu Khristu Ambuye" (2 Akorinto 4:5). Khristu akhale gwero la utumiki uliwonse ndipo munthu asakwezedwe.

Zonse pa Utumiki zidziyendera limodzi

Kulalikira kodzozedwa, kodzazidwa ndi Mzimu Woyeria kumachokera ku kumudziwa ndi kuyenda ndi Mpulumutsi komanso kukhala wokhulupirika ku kuperekira mauthenga akumwamba amene ali owuziridwa kuchokera kwa Mulungu. Paulo ananena kuti kulalikira kwake si kunali kwa kuposa kwa mau kapena kwa nzeru. Iye analikira Yesu Khristu osati "ndi kuposa kwa mau, kapena kwa nzeru, ...koma m'chionetso cha Mzimu ndi cha mphamvu" (1 Akorinto 2:1-5). Pamene chiweruzo chili gawo Iofunikira la utumiki woona ndi wopatulika, maziko ake nthawi zonse adzikhala pa chikondi. "koma ndi kuchita zoona mwa chikondi tikakule m'zinhu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Khristu" (Aefeso 4:15). Atumiki ena amakhazikika kwambiri pa



chiweruzo mwakuti amataya kuzama ndi tanthauzo lenileni la uthenga wa chikondi. Ena amakhazikika pa kuwapangitsa anthu kuti amve kukoma ndipo potero amakanika kutumikira ku choonadi chenicheni chimene chimakuza ndi kuperekira moyo kwa mzimu umene uli woona. Nkofunikira kuti pa utumiki zonse zidziyendera limodzi.

Utumiki Wosamalira

Timoteo analangizidwa kuti: "lalikira mau; chita nao pa nthawi yake, popanda nthawi yake; tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi chiphunzitso" (2 Timoteo 4:2). Nkofunikira kuti mtumiki akhale wokhulupirika posawerengera mmene akumvera iyeyo kapenango mayeso amene akukumana nawo m'moyo. Atumiki ayenera akhale opirira ndi oleza mtima, ndipo afunefune chikondi, chimwemwe, kudziletsa ndi kudzichepetsa zimene Mzimu wa Mulungu amapereka potumikira. Mtumiki amene wayenerezewa adzakhalapo kuti alimbikitse ndi kuthandiza anthu mu zosowa zawo komanso zovuta zimene akukumana nazo (1 Atesalonika 5:14). Iye ayenera kukhala woleza ndi wokoma mtima, wosamalira gulu la nkhosa za Khristu popeza mwini wakeyo, amene ali Mbusa wamkulu, amasamalira anthu ake.

Utumiki wokonzekeratu

Monga mmene imakhalira ntchito iliyonse kapena mayitanidwe aliwonse, kuti ikhale yopambana, atumikiwo ayenera kuti adzipereke ku kuphunzira kwa Mau a Mulungu. "Uchite changu kudzionetsera kwa Mulungu wovomerezeka, wantchito wopanda chifukwa cha kuchita manyazi, wolunjika nao bwino mau a choonadi" (2 Timoteo 2:15). Nkofunika kuti "Izi uzisamatise; mu izi ukhale" (1 Timoteo 4:14-16). Atumiki ayenera kunena kuti "tilankhula ndi kukhazikika mtima kwakukulu" (2 Akorinto 3:12) ndipo alankhule zakuti anthu adziwe ndi kumvetsetsa mosavuta chifuniro cha Mulungu.

Utumiki Wokhulupirika

Mtumiki aliyense wa Ambuye wokhulupirika ayenera kukhala wokhulupirika ku masomphenya a kumwamba ndi mayitanidwe a Mulungu. Chisomo ndi chikondi cha Ambuye wathu Yesu Khristu ndi mphamvu komanso kudzodza kwa Mzimu Woyeria zikhale pa inu. Amen.

—mws



Kodi kupatulidwa ndi chiyani?

Kupatulidwa ndiko kuvomereza mayitanidwe ndi zomuyenereza za mtumiki pamene atumiki anzake odzodzedwa amusanjika manja. Paulo analangiza Timoteo kuti "nukaike akulu m'midzi yonse" (Tito 1:5). Kupatula kutanthauza kusankha, kulongsola ndiponso kuyika mu mndandanda. Paulo anawuza Timoteo kuti "ukoleze mphatso ya Mulungu, ili mwa iwe mwa kuika kwa manja anga" (2 Timoteo 1:6). Pali zitsanzo zina kuchokera m'Malemba zimene zikuonetsera kuti kupatula ndiko kusankhidwa kwa atumiki kuchokera kumwamba komanso kuvomerezedwa pamene mpingo umudzoza ndi kumupatula mtumikiyo ku ntchito yapaderadera.

Taganiziani za pa Machitidwe 13:2-4. "Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala chakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Barnabasi ndi Saulo ku ntchito imene ndinawaitanirako.

Pamenepo, mmene adasala chakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke. Pamenepo iwo, "otumidwa ndi Mzimu Woyera..." zikuchita kuonekeratu kuti ndi Mzimu Woyera amene amapereka mphatso, amayitana, amayenereza komanso kutumiza atumiki.

Alaliki ndiponso antchito a Ambuye akuyenera kusankhidwa ndi Ambuye ndipo adzozedwe ndi mphamvu za Kumwamba komanso ulamuliro.

Kupatulidwa ndilo dzina limene Baibulo limagwiritsa ntchito pofuna kunena za mchitidwe wovomereza pomusanjika manja munthu, zimene Mzimu Woyera anasankha kale ndi kuvomereza.

Mbale Ostis Wilson analemba izi pa mutu umenewu mu zolemba zake zotchedwa *Faith and Victory* za m'mwezi wa December 1979.

Ndi zoona ndithu kuti mtumiki aliyense akhoza kuona kumasuka pamene akutumikira komanso kugwira ntchito mwabwino lomwe pamene akudziwa kuti ali ndi chivomerezo, chithandizo, chisamaliro ndi chilimbikitso cha atumiki ena amene iye amagwira nawo ntchito komanso oyera mtima onse. Munthu kuti apambane pogwira ntchito ya "Ukuluwampingo" kapena "Woyang'anira" m'magawo onse a mu mpingo, iye ayenera kupatulidwa posanjikidwa manja ndi atumiki ena odzodzedwa. Iye akhoza kulkalikira ndi kudyetsa nkhoa bwino lomwe popanda vuto ngakhale sanapatulidwe, komabe tikafika ku gawo la kulamulira ndi kulimbana ndi mavuto amene angapezeke mu mpingomo, iye adzagwira bwino ntchito komanso kulemekezedwa mu maweroz ake pamene mpingo ndi anthu wonse amene akutumikira nawo amuvomereza kwathunthu.

Kodi ndani ayenera kupatulidwa?

Mtumiki amene akuyembekezeaka kupatulidwa ayenera kukwaniritsa zomuyenereza kukhala woyang'anira zimene malemba amanena ndipo akhale ndi kudzodza komanso mayitanidwe pa moyo ndi utumiki wake. Iye ayenera kukhala chitsanzo cha moyo wa chiyero, wokhazikika mu chiphunzitso, ndipo wofanafana ndi Christu m'zochita zake. Mtumiki amene ali watsopano, ngakhale akhale wa zaka zotani komanso chidziwitso chochuluka bwanji, asapatulidwe mwansanga, komatu apatsidwe nthawi kuti adziwonetse yekha mu utumiki wake mwa Ambuye.

"Mau amaphunzitsa kuti mtumiki asapatulidwe mpakana ataonetsa kuti ndi woyeneradi. Mau akuti 'Asakhale woyamba utumiki kumene' akutiwonetsa kuti tiyenera kusalalitsa ndithu tisanamupatule munthuyo. Ngakhale izi zili choncho, tisatengeno nthawi yayitali tisanawapatule atumikiwa" (Carver, Cecil. *Church of God Doctrines*).

Kupatulidwa ndi chinthu chofunikira kwambiri ndipo chiyenera kuonedwa mwa umulungu. Paulo pa 1 Timoteo 5:22 anapereka malangizo akuti "Usafulumira kuika manja pa munthu aliyense, kapena usayanjana nazo zoipa za eni..." Ngati mkuluwampingo apatula mtumiki amene ali wosayenera, iye akutenga nawo gawo la kusayenerako povomerezana nawo utumukiyo. Mtumiki asagonjere ku

zofuna za ena kuti apatule munthu ngati palibe chitsimikizo ndi chivomerezo chenicheni kuchokera kwa Mzimu Woyera.

Kodi njira yoyenera kutsatidwa pofuna kupatula anthu ndi yotani?

Ngakhale kuti akulu ampingo awiri kapena atatu akhoza kuhala ndi ulamuliro wopatula wina wake, chikhalidwe cha kudzodza chimaonetsera kuti payenera kuhala kutsimikizika ndi kuvomereza kwa utumikiyo komanso mpingo wonse. Chifukwa cha ichi, kupatulidwa kusachitike mobisika koma mowonekera ndi chivomerezo cha gulu la akulu ampingo.

Ndi udindo wa wa abusa kapena atumiki ena amene akugwira ntchito limodzi ndi atumiki amene sanapatulidwe kuti awakonzekeretse kenaka ndi kuwaperekwa kwa gulu la akuluampingo kuti tsopano akhoza kupatulidwa. Ndi chinthu chanzeru ndthu kumufufuza nd kumufunsa mafunso mtumiki amene akuyenera kudzozedwa. Mukhoza kufunsa mkazi wake, komanso anthu amene iye amawatumikira ngati iye ali wokhazikika, wolimba mtima komanso kuti palibe mavuto aliwonse amene ali obisika. Chimakhala chinthu chodala kwa anthu a Mulungu komanso umboni wakuti Mzimu Woyera akugwiradi ntchito pamene mupanga mwambo wopatula mtumikiyo pamaso pa mpingo wonse.

Kupatulidwa ndi chinthu cha uzimu ndipo ndale kapena kukometsera kwina kulikonde zisalowererrepo. Kupatulidwa sikunalemekezedwe kapena kupatsidwa ulemu wake woyenera, ngakhale chili chiphunzitso chochokera m'Baibulo chimene chikadali chofunikira kuti mpingo walero uyende bwino. Kupatulidwa kuyenera kupatsidwa ulemu. Akulu ampingo amene anapatulidwa kale ayenera kulemekezedwa chifukwa cha ntchito zavo komanso chifukwa cha ulamuliro wawo mwa Mzimu Woyera.

—mws



KODI MUKUDZIWA?

Kafukufuku wa zimene Abusa akukumana nazo pa utumiki wao m'dzikoli

75% ya abusa amanena kuti amatopa kwambiri.

91% ya abusa anafika polema nawo mpaka kufuna kuwusiya utumiki.

70% ya abusa kawirikawiri amalimbana ndi nkawa.

70% ya abusa alibe munthu amene akhoza kumutchula kuti ndi mnzawo wapamtimi.

70% ya abusa amanena kuti malipiro awo ndi ochepta kwambiri.

80% ya abusa amakhulupirira kuti utumiki wao wapangitsa kuti mabanja awo asayende bwino.

33% ya abusa amanena kuti kukhala mbusa ndi chinthu chovuta kwambiri.

(*Kafukufuku ameneyu wachokera pa:: Fuller Institute, Leadership Journal 2013, Schaeffer Institute.*)



Umunthu wa Akuluampingo

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Si kuti tili okwanira pa ife tokha, kuyesera kanthu monga mochokera mwa ife tokha; kukwanira kwathu kuchokera kwa Mulungu; — 2 Akorinto 3:5

Kukhala mmodzi mwa akulu ampingo ndi mayitanidwe a mtengo wapatali. Atumiki ayenera kukhala oyenerezewa, atsogoleri auzimu ndi achitsanzo; ndipo mpingo wa okhulupirira udziwachitira umboni ndipo udzipereka ulemu ku udindo wao umene Mulungu anawapatsa. Nkofunikira kwambiri kukumbukira kuti anthu ndi amene amapanga gulu la akuluampingo. Atumiki a Mulungu si makina auzimu ayi komatu ndi anthu amene ali olephera m'magawo ena. Iwo ali ndi mmene amamvera, ali ndi zofooka, amalakwitsa, ndipo nthawi zina nzeru zimawaperewera. Iwo amayesedwa, amakhumudwa ndipo zina akhoza kumva kutopa zedi pa utumiki wao. Nkofunikira kwambiri kuti anthu aumvetsetse utumikiwo ndipo azindikire kuti atumikiwo ndi anthu, nawapatse chikondi ndi chisamaliro chonse.



Atumiki paokha si okwanira ndipo sangakwanitse kugwira ntchito ya Mulungu popanda mphamvu ndi kuthekera kwa Mzimu Woyera. Chikwaniro chao chili mwa Mulungu. Nthawi zambiri anthu amayembekeza udindo ndi mpando wa utumiki kuti uchotse zonse zimene zimatipanga kukhala anthu. Pamene mtumiki weniweni azindikira kuti iye ndi munthu ndithu zimamuthandiza kukhala wodzichepetsa ndi wodalira pa Ambuye.

Atumwi komanso atsogoleri a uzimu a m'mbuyomu anali ndi zofooka zawo popeza anali anthu, koma izi sizitanthauza kuti timapeputsa ntchito imene Mulungu anagwira kudzera mwa iwo kapena pakati pawo. Chokhumba chathu ndicho chakuti mwana aliyense wa Mulungu ndiponso mpingo wonse ulemekeze ndi kupereka ulemu kwa atumiki awo amene ali odzazidwa ndi Mzimu Woyera — pozindikira za umunthu wa akuluampingo.

—mws